

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

MOTSOGOZEDWA NDI M'BUSA

Kodi nditani? Kodi ndidzikhala kuno kapena ndisamuke? Kodi ndipitirize maphunziro anga? Ndi ntchito yanji yomwe ndikuyenera kudzagwira pamoyo wanga? Kodi munthuyu ndi amene ndikuyenera kukwatirana naye? Kodi ndilowe mpingo wanji? Kodi chabwino ndi chiyani? Kodi Mulungu amafuna kuti ndikhale motani ndipo amafuna kuti ndidzichita chiyani? Kodi njira yabwino yochitira zinthu ngati imeneyi ndi yotani? Sindikudziwa momwe ndingayankhire chobetchera chimene chili m'moyo mwanga. Ndili wokutidwa mu chisokonezo.

Moyo ukhoza kukhala wodzaza ndi mafunso, chisokonezo, ndi zisankho zambiri zofunika kuti tizipange. Zisankho zina zimakhala zazikulu kwambiri ndipo zimakhalsanso ndi zotsatira zazikulu; ndipo zina zimasinthanso mmene moyo wanu udzakhalire. Nkhani yabwino ndiyakuti simuyenera kukumana ndi zovuta izi nokha kapena mwanzeru zanu.

Mulungu amakhudgidwa kwambiri ndi moyo wanu ndipo ali ndi dongosolo lapaderadera ndi inu. Mulungu amalingalira kwambiri za moyo wanu wauzimu, komanso amakhudgidwa ndi chilichonse chimene chimakhudza moyo wanu.

Anthu ambiri amadalira nzeru zao, chidziwitso, kuganizira kwao, kapenanso malingaliro ao kuti zimenezi ziwatsogolere pazisankho zao. Kuchuluka kwa umboni, potsatira zimene zimawachitikira anthu amene timakhala nao, kumatsindika momveka bwino malemba



a pa Yereimiya 10:23 amene akuti, “Inu Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu sili mwa iye mwini; sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ake.” Anthu sanalengedwe kuti adzikhala opanda chitsogozo cha Mlengi wao. Kuchenjera kwa anthu ndi njira zao zimawatsogolera kuti apange zisankho zolakwika ndipo zotsatirapo zake zimakhala zoopsa. “Ilipo njira yooneka kwa mwamuna ngati yoongoka, koma matsiriziro ake ndi njira za imfa” (Miyambo 16:25). Pali Mpulumutsi

ndi bwenzi amene amadziwa zonse, amene amamvetsetsa zonse ndipo ali ndi mphamvu zonse komanso amafunitsitsa kuyenda nanu m'moyo uno. Ngati mumulola Iye, sadzakutsogolerani Kumwamba kokha, komanso adzakutsogolerani ndi kukuwongolerani mu zisankho zazikulu zomwe mukukumana nazo zimene zikhosha kupotoza moyo wanu. Mulungu ali ndi malingaliro abwino painu ndipo adzakutsogolerani bwino ziyangoyango ndi mavuto a moyo uno.

Ngakhale kuti pali zokayikitsa zambiri zomwe zingayambitse nkhawa ndi madandaulo, Mulungu samafuna kuti muyende mumdima kapena mu chisokonezo. Iye ndiye M'busa Wabwino amene amatitsogolera m'mpheapete mwa madzi odikha. Iye akufuna kukhala wosamalira amene ali bwenzi, ndipo koposa zonse kukhala Mpulumutsi amene adzayenda nanu ndi kupyola mu chigwa cha mthunzi wa imfa.

(Yapitirira pa tsamba 2)

“Mulungu amakufunirani zabwino ndipo adzakutsogolerani bwino pamavuto ndi m'avuto.”

Mau a Mkonzi

Kalozera wa Baibulo

Mmene Mungadziwire Chifuniro Cha Mulungu

Funso Yanko

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

3

4

5-8

9

10

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Chaputala 10 cha Yohane chimanena za Yesu Khristu ngati M'busa Wabwino. "Nkhosa zimva mau ake; ndipo aitana nkhoa za iye yekha maina ao, nazitsogolera kunjira. Pamene adatulutsa zonse nkhoa zimtsata iye; chifukwa zidziwa mau ake. Koma mlendo sizidzamsata, koma zidzamthawa; chifukwa sizidziwa mau a alendo" (v3-5).

Yesu amadziwa dzina lanu, ndipo amaona zisankho ndi ziganizo zomwe zili patsogolo panu. Liwu la Yesu lidzalowa m'maganizo ndi m'malingaliro kenaka ndi kupereka chitsogozo ndi chitonthozo. Yesu adzakutsogolerani, nadzakuonetsani njira, koma inuyo mumutsata? Ana a Mulungu amadziwa mau a M'busa ndipo adzamutsatira, nathawa mau ndi njira zina zonse. Anthu akamamvera mau a mlendo, adzapeza kuti akupitapitabe kutali ndi Khristu, ndi chiyeo komanso ndi Mau a Mulungu.

Pali nthawi zina pamene zikuoneka kuti Mulungu sakutsogolera, koma ngati mungadikire ndi kumvetsera, mau otonthoza a Mbusa adzalankhulanso ndikuongolera njira zachilungamo. Sitifunikira ndipo

**"Mulungu ali ndi malingaliro
abwino painu ndipo
adzakutsogolerani
bwino ziyangoyango ndi
mavuto a moyo uno."**

sitiyenera kudziikira njira tokha, chifukwa tidzalakwitsa. Ngati titsatira Khristu ndi njira yake, tidzafika kumapeto kwa mtendere ndi chigonjetso.

Ngati mufuna chifuniro cha Mulungu koposa zokhumba zanu ndi

zolinga zanu, Iye adzakuululirani inu mu nthawi yoyenera zomwe muyenera kuzidziwa. Mu kukhulupirika kwake, Mulungu wapatsa anthu mphatso zonse, zida, ndi zinthu zofunika zimene tingadziwire chifuniro chake changwiro pa miyoyo yathu. Tidzalakwitsa ngakhale pofunafuna chifuniro cha Mulungu, koma pamene tikukula mwa Ambuye ndi kuphunzira za Iye, tidzamvetsetsa mau ake ndi njira zake momveka bwino.

Yehova adzatsogolera ana ake. Iye adzatsogolera mwauzimu ndi kutithandiza kudziwa mmene tingakhaliro ndi moyo wokondweretsa Atate. M'zisankho zazikulu tingathe kutsogoleredwa ndi M'busa. Tisafike pamaso pa Iye kapena kupanga zisankho pa nthawi yathu, koma tiyeni timutsatire Iye mosamalitsa ndi moona mtima.

Ndi chitonthozo chachikulu kukhala mwa Mulungu panthawi ya kusamvetsetsana, maganizo otsutsana, ndi maganizo. Mulungu, mwa Mau ake, kudzera mwa Mzimu Wake Woyera, adzatsogolera ndi nzeru, kuzindikira, ndi chifundo. Tiyeni tidikire pa Ambuye ndi kutsogozedwa ndi M'busa. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ndipo Yehova anawatsogolera usana ndi mtambo njo kuwatsogolera m'njira; ndi usiku ndi moto njo, wakuwawalitsira; kuti ayende usana ndi usiku.

— Eksodo 13:21

Monga Yehova anatsogolera Aisraele mu mtambo njo usana ndi moto woyaka usiku kuti atsogolere njira, chotero Yehova adzakhalanso wokhulupirika kutsogolera ana ake lero lino. Mulungu sanatisiye ife tokha kuti tipeze njira yopitira Kumwamba. Sanatisiye tokha ku maganizo ndi nzeru zathu kuti tidzisankha zochita zimene zingasinthe kwambiri moyo wathu. Mulungu walonjeza kutitsogolera ndi kukhala nafe.

Mtolo wanga ulendo uno ndiko kugawana nanu Malemba ena a momwe mungadziwire chifuniro cha Mulungu. “Kodi ndingadziwe bwanji chifuniro cha Mulungu?” Limeneli ndi funso limene achinyamata ambiri komanso Akhristu amisinkhu yosiyanasiyana amafunsa. Palibe njira yotsatira yomwe ingabweretse yankho mofanana nthawi zonse. Komabe, Mulungu walonjeza kutitsogolera, ndipo anatipatsa malangizo ndi kutiuzana njira zopezera chifuniro chake. Kuphunzira kudziwa chifuniro cha Mulungu kumafunikira nthawi komanso chidziwitso. Ngakhale takhala tikutumikira Yehova kwa nthawi yaitali motani, Mulungu amafuna kuti tizimudalira.

Nthawi ya Mulungu ndi yapaderadera. Pakhala pali nthawi zomwe ndafunafuna Ambuye kuti anditsogolere kwa miyezi yambiri. Kenaka, Yehova akulankhula, ndipo nkhangungu ya chisokonezo imakanganuka. Monga nyimbo ina imanenera, “Ndimadziwa kumveka kokoma kwa liwu Lake.” Ndikuyamika kuti tikhoza kudziwa mau a Mulungu. Ndi losiyana ndi liwu lina lililonse.

Mu phunziro lathuli, tizukuta mwachidule njira zosiyanasiyana zimene Mulungu amaonetsera chifuniro chake pa miyoyo yathu. Sikuli kwanzero kutenga mboni imodzi yokha kuopera kuti tingalakwitse, koma ndi mboni ziwiri kapena zitatu, tingapite patsogolo mu chikhulupiriro ndi kutsimikizika.

Ngakhale ndikuchenjeza za ubweya wa chikopa, Yehova amazigwiritsabe ntchito nthawi zina. Ndikukumbukira kusintha kwakukulu komwe tinakhulupirira kuti Mzimu wa Mulungu akuyenda. Ndinapempha Mulungu kuti anditsimikizire ndi ubweya wa chikopa— chinthu chimene sichichitika mwachibadwa. Posakhalitsa, Mulungu anatsimikizira Mau ake ndi chitsogozo cha Mzimu Wake ndi kutsimikizira kwa ubweya. Izi zinali zisanachitikepo ndipo sizinachitikenso kuchokera pamene. Nthawi ina moyo wanga unali pampeni, ndipo ndinafunika umboni wochokera kwa Mulungu. Ngakhale kuti mau a Mulungu sanali kumveka, koma zinali ngati amamveka. Anandilankhula momveka bwino ngati mukukambirana. Izi zinali nthawi zapadera, ndipo ndapeza kuti nthawi zonse Mulungu samagwira ntchito mwanjira imeneyi. Komabe, Mulungu watitsogolera mokhulupirika ndi Mau ake ndi Mzimu wake kwa zaka zambiri, ndipo ndikuchitira umboni kwa inu kuti mukhoza kukhulupirira Yehova.

Kuyanjana ndi Mulungu tsiku ndi tsiku ndi chithonhozo ndi chitetezo pamene amatitsogolera panjira. Ndimalimbikitsa Mkhristu aliyense kuti apeze chitsogozo cha Ambuye pa ukwati, zachuma, kulera ana, kupembedza, ndi chisankho chilichonse chachikulu cha moyo. Mulungu adzakhalanso wokhulupirika kukwaniritsa lonjezo lake la chitsogozo ngati mutamufunafuna, kumudalira, ndi kumuyembekezera.

Michael W. Smith

April; 2022

Khulupirira

Yehova ndi mtima wako wonse; osachirikizika pa luntha lake; umlemekeze m'njira zako zonse, ndipo iye

adzaongola

mayendedwe ako. Miyambo 3:5-6



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Mmene mungadziwire chifuniro cha Mulungu

Kuwerenga Malemba: *Chifukwa chake musakhale opusa, koma dziwitsani chifuniro cha Ambuye nchiyani. — Aefeso 5:17*

Mwachidule: Mulungu wapereka zida ndi zinthu zomwe tingathe kudziwa ndikumvetsetsa chifuniro chake pa moyo wathu.

I. Ubwino wofunafuna chifuniro cha Mulungu

- A. Yeremiya 10:23 Si mwa munthu kuongolera mayendedwe ake.
- B. Miyambo 16:25 Njira za munthu ndi imfa.

II. Mungathe kudziwa chifuniro cha Mulungu

- A. Miyambo 3:6 Mulungu adzaongolera njira zako.
- B. Aefeso 1:8-9 Khristu amaulula chifuniro chake.
- C. Akolose 1:9 Kudziwa chifuniro cha Mulungu.

III. Chifuniro cha Mulungu kwa anthu onse

- A. 2 Petro 3:9 Onse ayenera kulapa.
- B. Aroma 12:1-2 Tsimikizirani chifuniro cha Mulungu.
- C. 1 Petro 1:15-16 Khalani oyera m'zochita zonse.
- D. 1 Petro 2:21-23 Tsatirani chitsanzo cha Khristu.
- E. 1 Atesalonika 4:3 Chiyeretso.
- F. 1 Atesalonika 5:16-18 Kondwerani, pempherani, thokozani.

IV. Momwe Mulungu amaululira chifuniro chake

A. Mau a Mulungu

1. Salmo 119:105 Kuunika kwa panjira pathu.
2. 2 Timoteo 3:15-17 Zopindulitsa pa malangizo.

B. Mzimu Woyera

1. Yohane 16:13 Iye adzatsogolera m'choonadi chonse.
2. Aroma 8:14 Kutsogozedwa ndi Mzimu.
3. Yesaya 30:21 Makutu ako adzamva mau.

C. Liwu la Mulungu

1. Mateyu 17:5 Mulungu amalankhula kuchokera mu mtambo.
2. Machitidwe 8:26 Mngelo wa Ambuye alangiza Filipino.

D. Zida za Anthu

1. Aefeso 4:11-13 Utumiki.
2. Ahebri 13:17 Gonjerani ku utumiki wa Mulungu.
3. Miyambo 11:14 Kufunikira kwa uphungu.

E. Chisamaliro

1. Aroma 8:28 Zinthu zonse zimayendera limodzi.
2. Machitidwe 16:6-7 Zolinga za Paulo zinalephereka.

F. Ubweya wa Chikopa

1. Oweruza 6:36-40 Gideoni aika chikopa cha nyama.
2. Mateyu 12:38-40 Chidzudzulo pofunafuna chizindikiro.

G. Masomphenya ndi maloto

1. Machitidwe 2:17 Mzimu adzapereka masomphenya ndi maloto.
2. Mateyu 2:13 Mngelo akuchenjeza Yosefe.
3. Machitidwe 10:9-10, 19-20 Masomphenya a Petro. Kutsimikiziridwa ndi Mzimu.

V. Mmene Mungafunire chifuniro cha Mulungu

A. Fufuzani ndi chikhumbo

1. Mateyu 6:33 Choyambayamba funani.
2. Salmo 143:10 Ndiphunzitseni kuchita chifuniro chanu.
3. Salmo 25:4-5, 9 Munditsogolere m'choonadi chanu.
4. Miyambo 3:5-7 Vomerezani Mulungu.

B. Pempherani mwachindunji ndi chikhulupiriro

1. Yakobo 1:5-6 Pemphani nzeru m'chikhulupiriro.

C. Yandikirani kwa Mulungu

1. Hoseya 6:3 Pamenepo tidzadziwa.
2. Yakobo 4:8 Yandikirani kwa Mulungu.

D. Mvetserani

1. Salmo 46:10 Khalani chete.
2. Yakobo 1:19 Khalani ofulumira kumva.

E. Dikirani moleza mtima

1. Salmo 27:14 Yembekezerani Yehova.

F. Gonjerani ku chifuniro cha Mulungu

1. Mateyu 23:37 Inu simunafuna!
2. Luka 22:42 Osati chifuniro changa.

VI. Kumvera

- A. Aefeso 6:6-7 Kuchokera mu mtima.
- B. Yesaya 1:19 Wofuna ndi womvera.

Kumaliza

Ndipo dziko lapansi lipita, ndi chilakolako chake: koma iye amene achita chifuniro cha Mulungu akhala ku nthawi zonse.

— 1 Yohane 2:17



MMENE MUNGADZIWI CHIFUNIRO CHA MULUNGU

Ndi chikhumbo ndi cholinga cha Mulungu kulankhula ndi ana ake. Iye walonjeza kutitsogolera ndi kutitsogolera, ndipo ndizotheka kudzera mu mphatso zaumulungu ndi zida za Mzimu kuti aliyense payekha adziwe chifuniro cha Mulungu pa moyo wathu. Ndikofunikira kuti tipambane mwauzimu kuti tikhale anzeru ndi kumvetsa “chimene chili chifuniro cha Ambuye” (Aefeso 5:17).

Mulungu amafuna kuwulula chifuniro chake

Malonjezo a Utsogoleri

Malonjezo a Mulungu ndi otsimikizika ndi ogwira ntchito kwa aliyense mu m'badwo uno amene amakwaniritsa chikhalidwe. Lemba la Miyambo 3:6 limati: “Umlenzeke m'njira zako zonse, ndipo iye adzaongola mayendedwe ako.” Ngati mwana wa Mulungu avomereza Mulungu ndi kumpatsa Iye ufulu ndi malo ogwirira ntchito, Iye adzaulula chifuniro chake chaumulungu ndi dongosolo lake. Zinsinsi ndi mafunso a moyo akhoza kuyankhidwa pamene Khristu “anatizindikiritsa ife chinsinsi cha chifuniro chake, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa Iye” (Aefeso 1:9). Pamene kuli kwakuti dziko linganyoze ndi kunyodola Akhristu, oyera mtima a Mulungu angadalire ndi kupumula mwa Ambuye, “kuti mukadzazidwe ndi chizindikiritso cha chifuniro chake mu nzeru zonse ndi chidziwitso cha mzimu” (Akolose 1:9). Ngakhale kuti anthu pa dziko pano akhoza kunyoza ndi kunyodola Akhristu, anthu oyera a Mulungu akuyenera ndi kupumula mwa Yehova. Ndi chithonhozo ndi nyonga zotani nanga kulimbana ndi zovuta ndi mavuto a moyo ndi chidziwitso chakuti Mulungu mwa nzeru zake zopanda malire adzatsogolera m'njira yoyenerera kukhoza kwathu kumvetsetsa chifuniro chake. Zisankho zazikulu m'moyo zingakhazikike m'chidziwitso ndi mphamvu za Mulungu m'malo mwa nzeru za dziko lino ndi kutengekatengeka kwa maimvaimva komanso za m'malingaliro.

Chifuniro chonse cha Mulungu

Mulungu ali ndi chifuniro pa anthu onse pamodzi ndi chifuniro chapadera ndi dongosolo la munthu aliyense. Dongosolo la Mulungu pa munthu silidzaphwanyika kapena kupititsa patsogolo chifuniro chake monga momwe zalongosoledwera mu malembo. Chotero,

chifuniro cha Mulungu nthawi zonse chiyenera kukhala maziko pamene munthu amafunafuna chitsogozo ndi chitsogozo chaumwini. Mulungu “wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa” (2 Petro 3:9). Monga momwe Mulungu amafunira kuti munthu aliyense apulumutsidwe ku uchimo, ndi chifuniro chakenso kuti “musafanizidwe ndi makhalidwe a panso pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuniro cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwirowi” (Aroma 12:1-2). Anthu amene amapempherera chifuniro cha Mulungu ndi utsogoleri m'miyoyo yao amapemphera pachabe ngati sangayambe kudzipereka wokha ku chifuniro chonse cha Mulungu. Mulungu sali wokakamizika kuyankha mafunso amene kawirikawiri amabweretsa kupsinjika m'maganizo ndi kuvutika ngati munthu poyamba sali wofunitsitsa kugonjera ku chifuniro chake chimene chavumbulutsidwa momveka bwino m'Malemba Opatulika.

Ndi chifuniro cha Mulungu kuti ana ake akhale “oyera m'makhalidwe anu onse” (1 Petro 1:15). Wina sayenera kupempherera chitsogozo pa nkhani yomwe imawayandikiza ndi dziko lapansi komanso ndi kuwatalikitsa ndi Mulungu, chifukwa chimenecho SI chifuniro chake. Chifuniro cha Mulungu ndi chakuti kuti ife titsatire chitsanzo cha Mwana wake, Yesu, potengera chikhalidwe chake cha kusachimwa, chiyero, kukhululuka, ndi chikondi (1 Petro 2:21-23). Ndi chifuniro cholembodwa cha Mulungu mu 1 Atesalonika 4:3 kuti tiyeretsedwe (olekanitsidwa ndi dziko lapansi kuti tigwire ntchito ya Ambuye basi). Tiyenera kukondwera, kupemphera, ndi kuyamika, popeza ichi ndi “chifuniro cha Mulungu mwa Khristu Yesu kwa inu” (1 Atesalonika 5:16-18).

(Yapitirira pa tsamba 6)

Zida zodziwira chifuniro cha Mulungu

Mulungu wapereka zida zingapo ndi mphatso zomwe tingawiritse ntchito pofuna kudziwa ndi kuphunzira chifuniro chake chaumulungu kawirikawiri komanso makamaka mafunso m'miyoyo yathu. Mulungu wapereka mboni ziwiri padziko lapansi zimene zimachitira umboni za Iye komanso chifuniro chake zimene zili Mau ndi Mzimu.



“Mulungu akalankhula kudzera m’Mau ake kapena kudzera mwa Mzimu wake, pamakhala chiwalitsiro chachindunji ndi liwu ku khutu la uzimu wa munthu amene sakayika konse kuti liwulo linali la Mulungu.”

1. Mau a Mulungu

Salmo 119:105 limanena kuti: “Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga.” Baibulo ndi buku la malangizo a mmene tingakhala pa moyo waumulungu. Ilo limayankha mafunso ambiri amene anthu amakhala nawo, osati okhudza zauzimu zokha, komanso okhudza zinthu munga zabanja, kulera ana, zachuma ndi zina zotero. Mau a Mulungu ndi chida cha mtengo wapatali chopezera pofuna kuzindikira chifuniro cha Mulungu, koma zimagwiritsa nthawi ndi khama pofuna kuwaphunzira ndi mtima wotseguka ndi malingaliro. Malemba “apindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m’chilungamo” (2 Timoteo 3:15-17). Mulungu akhoza kuuzira mwachindunji lemba limene limapereka yankho kwa wolifunafunayo. Cholakwika chikhoza kuchitika pamene lemba lina latanthauziridwa molakwa kapena lagwiritsidwa ntchito molakwa pa nkhani inayake. Anthu amene akufuna

kupita kwinakwake angapeze vesi limene limawauza kuti “pitani.” Akhozanso kupeza lemba lina limene limati “khalani kunyumba.” Anthu amene amatengera zinthu pamgong’o amapotoza malemba pofuna kukwaniritsa zolinga zaozao kunja kwa chifuniro cha Mulungu. Komabe, Mulungu adzachita ndipo amagwiritsa ntchito Mau ake kupyolera mu kuwuziridwa kwa Mzimu wake pofuna kupereka chitsogozo chapadera kwa miyoyo yona mtima imene ikufunafuna mayankho.

2. Mzimu Woyera

Mulungu anapereka mphatso yodabwitsa ya Mzimu Woyera kwa ana ake. Mzimu Woyera anabwera “kudzakutsogolerani m’choonadi chonse” (Yohane 16:13), ndipo ana a Mulungu “amatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu” (Aroma 8:14). Zimatenga nthawi kuti tiphunzire mmene Mzimu Woyera amatsogolerera, amaongolerera, ndi kuuzirira. Pofunafuna Mulungu, pali chinthu chokoma chimene chimachitika pokhala nalo khutu ndi “kumva mau kumbuyo kwa iwe, akuti, Njira ndi iyi, yendani inu m’menemo” (Yesaya 30:21). Pamene Mzimu Woyera akutsogolera, amachita izi kuchokera mkati mwa moyo ndipo ndi wosiyana kwambiri ndi malingaliro a m’maganizo omwe amabwera ndi kupita. Iye amagwirira ntchito kupyolera mu kuwuziridwa ndi kulemedwa kwa mumtima, ndipo pamene alidi Mzimu Woyera, utsogoleri wake umakhala wooneka komanso wosaphonyeka. Mzimu Woyera sadzayankhula konse kosiyana ndi Mau a Mulungu, ndipo onse awiri adzagwirizana nthawi zonse. Muyeso waukulu podziwa chifuniro cha Mulungu ndiko kutenga Mau ndi Mzimu kuti agwirizane pamodzi ndi mboni zina zocheperapo.

3. Liwu la Mulungu

Nthawi zina Mulungu amalankhula ndi mau omveka, munga pamene analankhula kuchokera mumtambo kwa ophunzira pa Phiri la Chiwalitsiro, kuti: “Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera; mverani iye” (Mateyu 17:5). Mngelo wa Ambuye analankhula ndi Filipo namuuza kuti apite ku Gaza (Machitidwe 8:26).

Ngakhale zingaoneke ngati zophweka kuti Mulungu alankhule momveka, Mulungu akalankhula kudzera m’Mau ake kapena kudzera mwa Mzimu wake, pamakhala chiwalitsiro chachindunji ndi liwu ku khutu la uzimu wa munthu amene sakayika konse kuti liwulo linali la Mulungu.

4. Zida za anthu

Nthawi zambiri Mulungu amagwiritsa ntchito anthu ena kuchitira umboni Mau ake ndi Mzimu Wake kwa wofunafunayo. Ngakhale kuti pali mau ambiri padziko lapansi, mtumiki weniweni ndi phungu wa Ambuye adzalankhula zomwe zimagwirizana ndi mboni ziwiri zoyambirira. Mulungu anaika utumiki m'thupi kuti ufikitse ungwiro ndi kumangirira oyera mtima (Aefeso 4:11-13). Pamene pali mafunso ofunikira chitsogozo cha Mulungu, iye kawirikawiri amagwiritsira ntchito atumiki ake otumikira kutsimikizira chifuniro chake. "Popanda upo wanzeru, anthu amagwa" (Miyambo 11:14). Ndi njira yabwino kwambiri yopezera uphungu waumulungu pa zosankha zosintha moyo, makamaka pankhani zauzimu.

5. Chisamaliro

Kupereka kwa Mulungu ndi njira ina imene Mulungu amaululira chifuniro chake. Izi zikugwira ntchito pakutsekuka kowoneka kwachilengedwe ndi kutseka kwa zitseko. Ngati wina akufunafuna chitsogozo cha Ambuye pakati pa mipata iwiri, ndipo mwayi umodzi utsekeka, izi zikusonyeza chisamaliro cha Mulungu. "Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino" (Aroma 8:28). Ngakhale kuti Mulungu sagwiritsa ntchito ulamuliro wake yekha, mwana wa Mulungu akhoza kukhulupirira kuti Mulungu akutsogolera ndi kulola zikhalidwe zimene zidzakwaniritsa chifuniro chake m'miyoyo ya anthu ake. Mapulani amatha kusokonezedwa ndi zikhalidwe, ndipo ndikofunikira kuphunzira kusiyana pakati pa zovuta zomwe ziyenera kugonjetsedwa komanso zotchinga zomwe zimafunikira kutsogolera njira ina.

6. Ubweya wa chikopa

Mu chipangano Chakale, Gideoni anaika ubweya wa chikopa pamaso pa Yehova kuti adziwe maganizo a Mulungu (Oweruza 6:36-40). Ngakhale kuti Mulungu amalemekeza ubweya wa chikopa nthawi zina, Khristu anadzudzulanso Ayuda pa Mateyu 12:38-40 chifukwa chofunafuna chizindikiro choti akhulupirire. Chizindikiro



chikapanda kubwera, sichimasonyeza chifuniro cha Mulungu. Ubweya wa chikopa suyenera kugwiritsidwa ntchito kawirikawiri komanso ndipo tiugwiritse mosamala komanso motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Sizili kwa ife kumuuzza Mulungu m'mene angaonetsere chifuniro chake.

7. Masomphenya ndi Maloto

Chimodzimodzinsu, masomphenya ndi maloto ayenera kugwiritsidwa ntchito mosamala osati moonjeza. Machitidwe 2:17 amanena kuti pamene Mzimu Woyera anatsanuliridwa kuti "anyamata anu adzaona masomphenya, ndi akulu anu adzalota maloto." Yosefe analandira malangizo m'maloto kuti athawire ku Aigupto pa Mateyu 2:13. Mulungu anaphunzitsa Petro phunziro la kuvomereza amitundu m'masomphenya okhudza kudya nyama zodetsedwa (Machitidwe 10:9-10). Ndizofunikira kudziwa kuti Mzimu Woyera anatsimikizira loto kwa Petro mu vesi 19-20: "Pamene Petro analingirira masomphenyawo, Mzimu anati kwa iye.... Nyamuka... ndipo upite nawo, wosakayika konse; pakuti Ine ndawatuma iwo." Mulungu akamalankhula kudzera m'maloto ndi m'masomphenya, nthawi zonse amakhala mogwirizana ndi mboni zina. Tanthauzo lake lidzakhala lomveka bwino osati losokoneza, zosamveka bwino ngati loto lachilengedwe. Samalani poyesa kumasulira ndi kuika Mulungu m'maloto aliwonse.

M'mene mungafunire chifuniro cha Mulungu

Cholinga cha Mulungu komanso kufunitsitsa kwake ndiko kuulula chifuniro chake ndiponso kutsogolera anthu ake. Chifuniro chake sichiyenera kukhala chinsinsi m'mbali zonse za moyo. Komabe, nthawi zambiri Mulungu samayankha mafunso athu ndi mabingu akumwamba. Pali njira yovomerezeka imene timasakasakira chifuniro cha Mulungu pamene tikugwiritsa ntchito maumboni ndi zida zimene watidalitsa nazo.

1. Chilakolako ndi kufunitsitsa

Chifuniro cha Mulungu chikuyenera kuti chidzifunidwa ndi chikhumbo chachikulu chofuna kukondweretsa Yehova. "Muyambe mwafuna Ufumu wa Mulungu, ndi chilungamo chake; ndipo zonsezi zidzaonjezedwa kwa inu" (Mateyu 6:33). Anthu amene saika Mulungu patsogolo m'mbali zonse za moyo, nthawi zambiri sadzalandira mayankho monga momwe amafunira. Payenera kukhala chikhumbo cha kuphunzira ndi mzimu womvera. "Mundidziwitse njira zanu, Yehova; mundiphunzitse mayendedwe anu" (Salmo 25:4-5). Mulungu adzatsogolera ofatsa (Masalimo 25:9) ndipo adzaongolera njira ya wofunafuna ndi mtima wonse (Miyambo 3:5-7). Yankho likapanda kubwera, limakhala ngati uthenga wa palamya umene

(Yapitirira pa tsamba 8)

(Kuchokera pa tsamba 7)

watumizidwa kenaka ndikusochera chifukwa chakuti pali ziyangoyango zambiri munjira. Khalani ndi malingaliro osasokonezeka ndipo funafunani Mulungu ndi mtima wotseguka ndi woona mtima.

2. Pempherani mwa chikhulupiriro

“Ngati wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye. Koma apemphe ndi chikhulupiriro, wosakayika konse” (Yakobo 1:5-6). Pamene pafunika kuti tipange zisankho zazikulu pamafunikanso chitsogozo cha Mulungu, pamene pemphererani chosowa chenichenicho ndipo mukhale ndi chikhulupiriro chakuti Mulungu adzayankha panthawi yoyenera. Kusautsika ndi kudera nkhaba kungachepetsedwe pamene munthu aphunzira kukhulupirira ndi kupemphera.

3. Yandikirani kwa Mulungu

Mau a pa Hoseya 6:3 amatiphunzitsa mfundo yofunika kwambiri yokhudza kudziwa chifuniro cha Mulungu. “Tidziwe tsono, tilondole kudziwa Yehova.” Mukadziwa munthu nthawi yaitali, mumadziwanso bwino za chikhalidwe chake, maganizo ake, zomwe amakonda, zolinga zake, ndi chifuniro chake. Ndi chimodzimodzinso ndi Mulungu. Pamene tikuyandikira kwa Mulungu, timakhala kutali ndi dziko. Timaona ndikumudziwa Khristu mochulukira chifukwa cha Iye mwini ndi chomwe Iye ali. Izi zimatithandiza kumvetsetsa mau ake ndi chifuniro chake momveka bwino m'miyoyo yathu.

4. Khalani Chete ndi Kumvetsera

Pamene muli mu chisokonezo ndipo pamene chifuniro cha Mulungu sichidziwika bwino, imeneyi ndi nthawi yoti “Khalani chete, ndipo dziwani kuti ine ndine Mulungu” (Salmo 46:10). Yakwana nthawi yoti mukhale chete ndikuyamba kumvetsera mau ayeziyezi aja. Mulungu ndiye akuongolera zonse ndipo sadzasiya ana ake.

5. Dikirani Moleza Mtima

Pamene mukufunafuna chifuniro cha Mulungu, ana a Mulungu posachedwapa adzazindikira kuti Mulungu amagwira ntchito pa nthawi yosiyana ndi yao. Sakakamizidwa ndi nthawi yathu yomalizira zinthu kapena zofunika zathu. Komabe, Iye amasunga nthawi. Mulungu saulula zonse nthawi imodzi. Pa nthawi yodikirira kuti Mulungu aulule chifuniro chake, pali kukula kumene kukuchitika. “Yembekezani pa Yehova: limbikani mtima” (Salmo 27:14). Chifuniro cha Mulungu kawirikawiri chimakwaniritsidwa m'nthawi yathu yofunafuna ndi kudikirira. Pamene mukudikirira, musagwedezeke kapena kukhumudwa. Khalani okhulupirika pochita zimene mudziwa kuti Mulungu ayenera kuchita. Muloleni Mulungu alankhule momwe angachitire komanso panthawi yake, koma musatengere zinthu m'manja mwanu. Khulupirirani mwa Iye ndipo dikirani moleza mtima kuti Mulungu aulule chifuniro chake chaumulungu. Ngati simukumvetsetsa, dikirani.

6. Gonjerani ku chifuniro cha Mulungu

Ngakhale kuti Mulungu ndi wolamulira, analenga kuti akhale ndi ufulu wosankha. Chifukwa chake, chifuniro cha munthu chingasokoneze chifuniro changwiro cha Mulungu kuti chisakwaniritsidwe m'moyo wa munthu payekha pokhapokha ngati pali chosankha cha kugonjera ndi kutsatira chifuniro cha Mulungu. Yesu akanateteza Yerusalemu ndi kufuna kutero, koma iwo sanatero (Mateyu 23:37). Chifuniro cha Mulungu chiyenera kufunidwa ndi kuyesayesa kogwirizana kupereka zikhumbo zaumwini ndi zokonda m'dzanja Lake. Anthu ambiri amafunafuna madalitso a Mulungu pa zosankha zao popanda kumufunafuna poyamba kuti akwaniritse chifuniro chake. Tiyenera kupemphera monga Khristu: “Osati kufuna kwanga, koma kwanu kuchitidwe” (Luka 22:42). Ngati sitili ofunitsitsa kugonjera ku chifuniro cha Mulungu, kodi tikufuna chiyani?

Kuyenda m'moyo wa kumvera



Nkofunika kufunafuna chifuniro cha Mulungu pamene tikuyenda m'moyo wa kumvera m'magawo onse a moyo. Sitingayembekeze kuti Mulungu adzaulula cholinga chake m'gawo lina malinga ndi zofuna zathu ngati sitikumvera zimene tikudziwa kuti ndi chifuniro chake m'mbali zina. Pamene Mulungu waulula chifuniro chake, pamakhala dalitso lodabwitsa la kutsatira mwa kumvera ndi kuchita chifuniro cha Ambuye. “Ngati inu muli ofuna ndi omvera, mudzadya zabwino za dziko” (Yesaya 1:19).

Sikotheka kokha koma ndi chaulemerero chenicheni pamene tikhala pansu pa chitsogozo ndi kudzoza kwa Mulungu. Pamene tikonzezeretsa mitima yathu ndi kufunafuna Ambuye, tikhoza kudziwa komanso kuchita chifuniro chake. Kudziwa chifuniro cha Mulungu ndi chinthu chimene chimatenga nthawi ndi pamafunika kukula, choncho musataye

mtima. Pamene muli mkati momutsatira mudzadziwa Yehova, mudzaphunzira kuzindikira kumveka kodabwitsa kwa mau ake ndipo mukhoza kukhala ndi moyo ndi kuyenda pansu pa chitsogozo chake. Mulungu adzakutsogolerani ndi kukuwongolerani pa ulendo uno wa moyo. Malemekezo apite kwa Mulungu! ■



Kodi pali chifuniro cha Mulungu pa chisankho chilichonse chimene timapanga?

Mulungu ali ndi chidwi ndi moyo wathu chifukwa amatikonda. Iye ali chifuniro chapaderadera pa zinthu zauzimu ngakhale zinthu zimene zingakhudze mkhalidwe ndi ubwino wa miyoyo yathu. Komabe, pali zisankho zina zimene zili nkhani ya munthu aliyense payekha zimene Mulungu safuna kuchitapo kanthu. Kodi mumapaka penti woofiira kapena wa buluu? Kodi mumakwera basi kapena galimoto wamba? Kodi mudyamba mbatata kapena mpunga madzulo ano? Mulungu amatilola ife kuti titsatire zimene timakonda ndipo amalemekeza zisankho zathu pa zinthu zimene zimaoneka ngati zosafunikira kwenikweni. Ana a Mulungu ayenera kuchita chifuniro chawo mopanda mantha mkati mwa chifuniro chonse cha Mulungu. Koma ngati mu zisankho za zinthu zooneka zosafunikirazo Mulungu aonamo choopsa kapena chotchinga chinachake, tikhoza kumudalira kuti Iyeyo adzakhala wokhulupirika kuti ululira zimenezo pamene kuli kofunikira ndi koyenera kutero.

Kodi ndimasiyanitsa bwanji mau a Mulungu, maganizo anga, ndi Mdierekezi?

M'kupita kwa nthawi, malingaliro athu adzasinthana ndipo angasinthe chifukwa cha zimene mtima wathu wakumana nazo, koma liwu la Mulungu silidzasinthana. "Muli zolingalira zambiri m'mtima mwa munthu; koma uphungu wa Yehova ndiwo udzaimika." (Miyambo 19:21). Mamasulidwe a Baibulo lina amati: "Munthu mumtima mwake amakonzekera zambiri." Malingaliro athu omwe amabweretsa chisokonezo, kukayikira, ndi chipwirikiti. Mau a Mulungu amabweretsa mtendere, bata, ndi chitsimikizo ndipo amatsagana ndi mboni zina. Lemba la 1 Akorinto 14:33 limati: "Pakuti Mulungu sali Mulungu wa chisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima." Ngakhale izi zikunena za machitidwe a anthu mu utumiki wopembedza, pali choonadi chofunikira chakuti "Mulungu SALI woyambitsa chisokonezo." Pamene malingaliro aononga maganizo ndi kubweretsa chisokonezo ndi mafunso ambiri, tiyenera kuzindikira

kuti si mmene Yehova amachitira nafe. Pamene Mulungu alankhula, kumabweretsa mayankho komanso kuzindikira chifuniro cha Ambuye kuchokera mozamamo mkati mwa mzimu.

Nthawi zonse, liwu la Mulungu lidzakhala logwirizana ndi Mau Ake, ndipo Iye sadzatitsogolera m'njira yotsutsana ndi mfundo zokhazikika za choonadi. Ndikukumbukira zaka zapitazo ndinamva mtumiki wina amene poyamba anaphunzitsapo zosutsana ndi kukwatiranso. Iye anauza mpingo wake kuti Mulungu analankhula naye ndipo anamuza kuti safunikira kukhalanso wosakwatiwa ndipo akhoza kukwatiranso. Izi zinali zoonekeratu kuti sanali Ambuye, chifukwa zinali zosutsana ndi Malemba. Pamene malingaliro kapena chitsogozo zili zosiyana ndi Mau, tikhoza kuzindikira kuti sizinachokere kwa Mulungu ndi kudziwa kuti ndi kuganiza kwathu kapenanso kwa mdierekezi.

Nthawi zina pamakhala mafunso ngati liwu lamkati limachokera kwa Mulungu kapena mdani. Taganizirani za Petro pamene ophunzira ake anali m'mphepo ya namondwe. Iwo anachita mantha ndipo Yesu anadziwulula yekha. Komabe, Petro anayankha kuti: "Ambuye, ngati ndinutu, ndiuzeni ndidze kwa Inu pamadzi" (Mateyu 14:28). Yesu anatsimikizira zimenezi ndipo Petro anatha kuyenda pamadzi. Pamene Yehova alankhula, umboniwo udzatsimikizira zoonadi za zimene zinalankhulidwa. Mdierekezi ndi tate wa mabodza, ndipo tikhoza kuphunzira ndi kuzindikira mau ake onyenga.

Ngakhale pamene Satana anagwiritsa ntchito malemba pomuyesa Yesu, anatengak nunsu ya lemba linalake lomwe silinagwirizane ndi nkhanio. Pamene Mdyerekezi akulankhula, ngakhale akhoza kuvala zovala zachipembedzo, iye amalankhula za zinthu zimene zimatikokera ku zilakolako za thupi m'malo mwa zinthu zimene zingatisendezera kwa Mulungu.

Pamene Mulungu alankhula kwa ife za zolakwa, zolakwika, kapena tchimo, Iye adzaperekanso yankho ndi njira yothetsera vutolo. Pamene mdani alankhula, amatsutsa ndi kusokoneza maganizo ndi mzimu kuti abweretse kutsutsika popanda kupereka njira yowombolera. Anthu ambiri amakhala akutsutsidwa ndi Mdyerekezi ndipo amamva chisoni nthawi zambiri. Izi sizochokera kwa Mulungu, chifukwa ndi kutsutsika kosweka mtima kumene kuli koono, Mulungu amapereka yankho ndi mtendere umene umatsatirapo.



KODI MUKUDZIWA?

Mulungu amadzudzulidwa pa zinthu zambiri ndi anthu achipembedzo. Anthu ambiri amagwiritsa ntchito “mau a Mulungu” kulungamitsa ndi kufotokoza zisankho ndi makhalidwe awo. M’pofunika kuti Mulungu asagwiritsidwe ntchito ngati chinthu chonamizira kapena pongofuna kupeza pothawira pamene tikufuna kutsatira njira zathu, malingaliro, ndi zokonda zathu. Munthu aliyense payekha akuyenera kuvomereza zolakwa zake ngakhaleenso zolakwitsa zimene anachita pa kumvetsetsa za Yehova ndi chifuniro chake.



Mau a Nyengo Yake

NDIDZAKUTSOGOLERA NDI DISO LANGA

Ndidzakulangiza ndi kuphunzitsa iwe za njira ukayendayo; ndidzakupangira ndi diso langa. — Salimo 32:8

Mu dziko lodzala ndi mavuto ndi chisokonezo, kodi ndi lonjezo lodabwitsa ndi chithonhozo chotani nanga chimene Mulungu anapereka kwa Davide. Mulungu adzachitanso chimodzimidzi kwa ife lero lino. M’mafunso athu ndi m’zosowa zathu Iye amatitsimikizira kuti, “Ndidzakulangiza ndi kuphunzitsa iwe za njira ukayendayo.” Mulungu adzatiyendetsa munjira imene sitinayendemo. Iye adzakhala kapitawo ndi mtsogoleri wathu pamene sitidziwa njira yoti tipite. Iye adzakhala mphunzitsi wathu mu zovuta za moyo.



Adzakhala mlangizi mu nthawi ya chisokonezo. Iye adzakhala m’busa tikasokera. Iye adzakhala kuunika mundima wathu ndi chiyembekezo m’kusatsimikizika kwathu.

Sitingathe kuona za mtsogolo, ndiponso sitidziwa zimene tidzakumane nazo mawa. Sitikudziwa misampha ndi zoopsa zomwe zili patsogolo pathu. Yehova akutiya kuti: “Ndidzakutsogolera ndi diso langa.” Iye adzapita patsogolo pathu ndi kukaunguza ngati kuli zoopsa. Adzatisamalira bwino lomwe kuti atsimikize kuti njirayo ilibe zotsamwitsa. Ngati pali zotchinga, Mulungu adzaticweza kapena kutionetsa njira yozungulira kapena njira yopyoza. Ngati tipunthwa, Iye amadziwa ndipo adzasamula dzanja lake ndi kutigwira. Ngati mu umunthu wathu tataya njira yathu, Iye adzabwera kudzatifunafuna ndi kutitsogolera motetezeka kubwerera ku ubusa wake.

Ndife ofooka komanso tili osakwanira ndipo sitidziwa chomwe chili chabwino pa zisankho zambiri zomwe timakumana nazo pamoyo wathu. Yehova walonjeza kuti adzaticweza ndi kutithandiza. Iye adzationetsa njira ndi kutichotsera ziyangoyango pakati pa chisokonezo chathu. Diso lake lili pa ife. Mwana wa Mulungu sayenera kuda nkhwana kapena kuchita mantha. Izi zimabweretsa chithonhozo ndi chitetezo makamaka podziwa kuti Ambuye akundiayang’anira.

“Taonani, diso la Yehova liri pa iwo akumuopa Iye, pa iwo akuyembekeza chifundo chake” (Salmo 33:18). Mulungu amasamalira anthu onse, koma amapereka chisamaliro chapadera kwa amene amamulemekeza ndi kumukhulupirira.

Monga Mulungu amasamalira ngakhale mpheta imene yagwa, diso lake limakhala pa inu. Limba mtima msilikali mnzanga. Mulungu adzakutsogolera ndi kukufikitsa ku tsidya linalo mwamtendere. ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE